

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

Kalata yokondwerera zaka 10

CHOONADI CHOSASINTHIKA

Kalata ya Gospel Truth yakhala ikusindikizidwa ndi kufalitsidwa kwa zaka khumi tsopano. Kalata yoyamba inasindikizidwa mu July 2012. M'zaka 10 zapitazi, pachitika zinthu zambiri zazikulu komanso kusintha kwa anthu. Mphepo zamkuntho zingapo, zivomezi, ndi madzi osefukira a chigumula akhudza maiko padziko lonse lapansi ndikupha anthu ambiri ndipo chuma chimene chaonongeka chikhoza kukwana ma biliyoni ochuluka. Madera ambiri muli chilala, ndipo anthu akufa ndi njala. Mliri wa COVID wasintha kwambiri moyo wathuwu, ndipo anthu opsa 6 miliyoni amwalira.

Chikhalidwe cha umunthu chikuzilala mwansanga. Izi zikutsimikizika mwa zina ndi kuvomeredwa ndi kulimbikitsidwa ndi iwo amene amavomereza za maukwati a amuna kapena akazi okhaokha. Izi akuzifalitsa kudzera mwa atolankhani, mu masukulu, ndi m'madera ena onse. Pakhala pali zinthu zosintha zambiri ndipo zinthuzi zitha kuoneka zosasangalatsa. Kukwera kwa mitengo kwa katundu, kuchuluka kwa chiwongola dzanja kuposa kale, ndiponso mitengo yamafuta ikukwera kwambiri.

Nkhani yabwino ndi yotamandika ndiyo yakuti Mulungu ndi Mau ake sanasinthe. "Ine ndine Yehova, sindisintha" (Malaki 3:6). Ngakhale zinthu zikhale kuti zikusintha motani paliponse potizungulira ife, koma Mulungu sasintha konse. Ndi mdalitso waukulu kuti Uthenga Wabwino wa Choonadi ufikire pachimake patapita zaka khumi ukusindikizidwa. Mau a Mulungu amene Uthenga Wabwino wa Choonadi wakhala

ukuwasindikiza ndi kugawana nanu sanasinthe m'zaka khumi zapitazi. "Udzuwo unyala, duwa lifota; koma mau a Mulungu wathu adzakhala chikhalire" (Yesaya 40:8).

Maboma asintha, mautumiki abwera ndi kupita, nzeru ndi maganizo a anthu adzuka ndipo ena agwa, koma choonadi chikhalabe chokhazikika. Yesu anati, "Ine ndine njira, ndi choonadi, ndi moyo" (Yohane 14:6). Yesu akadali njira yokhayo yopitira Kumwamba ndipo njirayo ikadali yomveka bwino. Tsogolo limakhala lowala kwa mwana aliyense wa Mulungu komanso kwa mzimu uliwonse womwe uli ndi chikhumbo chokhala ndi moyo wa Mulungu.

Mwazi wa Yesu sunataye mphamvu zake, ndipo choonadi chikubweretsabe ufulu ku miyoyo imene yamangidwa ndi uchimo.

Tamandani Mulungu, pali chisomo chokhala ndi moyo woyera, ndipo mphamvu ya chisomo imaposa mphamvu ya uchimo. Ngakhale kuti padzikoli pali chisokonezo ndi chipwirikiti, kumbukirani mau a Ambuye wathu akuti: "Zinthu izi ndalankhula ndi inu, kuti mwa Ine mukakhale nao mtendere. M'dziko lapansi mudzakhala nacho chivuto, koma limbikani mtima; ndalingonjetsa dziko lapansi Ine (Yohane 16:33). "Mtima wanu usavutike, kapena usachite mantha" (Yohane 14:27).

Mosasamala kanthu za zopsinja ndi kusintha kwa dziko lathu lapansili, cholinga cha kusindikiza kalata ya Uthenga Wabwino wa Choonadi chidakali chimodzimidzi—chimene chili, kufalitsa Mau osasintha a Mulungu.



"Mau a Mulungu amene Uthenga Wabwino wa Choonadi wakhala ukuwasindikiza ndi kugawana nanu sanasinthe m'zaka khumi zapitazi."

Mau a Mkonzi

Mndandanda wa Nkhani

Ogwira Ntchito osiyanasiyana

Zimene zachitika

Kodi Mukudziwa?

3

4

5
Zithunzi za atumiki

6

7

Mau a Nyengo Yake

8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

Pitani pa Intaneti Patsamba lathu

www.thegospeltruth.org



Webusaiti ya Uthenga Wabwino wa Choonadi ili ndi makalata onse a Uthenga Wabwino wa Choonadi m'zinenero zisanu ndi chimodzi: Chingerezi, Chisipanishi, Chijeremani, Chiswahili, Chichewa, Chitamil ndi Chimalayalam.

Nkhani za m'mbuyo zimafotokoza za chiphunzitso pa mitu zosiyanasiyana. Izi zakhala zikugwiritsidwa ntchito monga mlozo wa munthu payekha kapena ngati gulu pamene akuphunzira Baibulo, koamnsa pa maphunzira a Baibulo a ophunzira akusekondale, ndi monga kalozera wamkulu ku ziphunzitso za mu Baibulo.

Mukatsegula fayilo ya PDF ya Gospel Truth mutha kufufuza pakudina nthawi imodzi zilembo za ctrl+F. Nkhani iliyonse imayikidwa padera mu blog yomwe mukhoza kufufuza zinthu zinanso.

***Lowani pa webusayiti kuti mulandire
zidziwitso za chotulukapo chotsatira
cha Choonadi cha Uthenga Wabwino
ndikuchipereka mwachindunji ku bokosi lanu!***

Tsekulani App

Kuchokera ku Google Play Store

App ya Gospel Truth ilipo kwa ogwiritsa ntchito pa mafoni ambiri okhala ndi intaneti. Kuti mupeze nkhani imene mukuyifuna mupite pamene pali chofufuzira.

Ntchito yokonza Baibulo la Chisipanishi ili mkati.



Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Ndipo mau a Ambuye anabukitsidwa m'dziko lonse. — Machitidwe 13:49

Pemphero lathu ndi chikhumbo chatu chinali ndipo chidakalipo lero kuti uthenga wosavuta wa Yesu Khristu ufalikire kumadera onse a dziko lapansi. Zipembedzo ndi mabungwe a anthu sizidzakhutitsa moyo wolakalaka. Pali kufunika kwakukulu kwa anthu kumva ndi kuwerenga chiphunzitso chosaipitsidwa, choyera ndi ziphunzitso za Mau a Mulungu.

Ndikuthokoza kwambiri Ambuye kuti tikukondwerera zaka khumi zakufalitsa Uthenga Wabwino wa Choonadi. Sikuti ndi zophweka kapena zosavuta, koma ntchito ya Mulungu siyopangitsa kuti zinthu zichitike mosavutikira; ndi kuyankha maitanidwe a Mulungu ndi kuchita chifuniro chake, mosasamala kanthu za mtengo wake. Ndikukumbukira zaka zoposa makumi awiri ndi zisanu zapitazo ndikufotokozera kufunika kwa kalata yonena za chiphunzitso yomwe ndikhoza kugawana ndi atumiki pa ntchito yolalikira uthenga wabwino. Panadutsa zaka zambiri pamene ichi chinatifikira kuchokera kwa Ambuye kuti tiyambe utumiki uwu.

Nayi nunsu ya Mau a Mkonzi a mu kalata woyamba wa Uthenga Wabwino wa Choonadi mu July 2012:

Kudzera mu zaka zambiri zotumikira pa dziko lino, ndazindikira kufunikira koyambitsa mautumiki ku maiko akutali kuti nawonso adziwe choonadi cha Mau. Sikuti ndikufuna kupeza anthu ambiri onditsatira kapena kuti wina wake alowe m'gulu lathu. Ndikufuna kuti anthu aphunzitsidwe ndi kulimbikitsidwa kukhala monga mpingo mu dera lao. Umodzi umabwera pamene anthu ayenda mu choonadi, koma potsogozedwa ndi Mzimu Woyera....Ndi chokhumba cha mkazi wanga komanso cha ine mwini kuti tidzikugawirani kudzera mmau olembedwa mu kalatayi zina mwa mfundo zoonza zopezeka mmalemba zimene zikhoza kuthandiza mitima yoonza kuti ikhazikike m'mau.

Kwa zaka khumi, Uthenga Wabwino wa Choonadi wakhala ukufalitsidwa miyezi itatu iliyonse. Mulungu wakhala wokhulupirika popereka utumiki amenewa kwa othandiza ndi odzipereka amene ali odabwitsa. Ndi chifukwa cha khama lawo, m'dziko muno komanso m'maiko ena zimene zapangitsa kuti utumiki umenewu ukule ndi kufikira anthu ambiri. Ndife oyamikira kwa iwo amene athandizira kusindikiza Gospel Truth ndi mapemphero komanso ndalama.

Pamene tikupita patsogolo mzaka khumi zikubwerazi zofalitsa, tifunafunabe mapemphero anu kuti mutakasidwe ndithu ndi kudzoza kwakukulu. Ambuye atsegule zitseko zambiri ndikupangitsa kuti choonadi chikagawidwe kwa anjala ndi miyoyo imene ili yokhumbitsitsa.

Ndi mtima woyamikira,

Michael W. Smith

July 2012

WOTSAGANA NAYE PA ULENDO

Pazaka zisanu zapitazi, Uthenga Wabwino wa Choonadi wakhala dalitsa lalikulu popititsa patsogolo uthenga wabwino pakati pa anthu olankhula Chitamil ku India ndi dera lonse la Asia-Pacific. Uthenga Wabwino wa Choonadi unapereka njira yowafikira anthu ochuluka kuposa momwe tikanakwanitsira tikanati tiwafikire paulendo wokawalalikira, ndipo kalatayi ili ngati mthenga wosalakwa komanso wowafikira chaka chonse ndi uthenga wabwino m'dera limene limadana kwambiri ndi Chikhristu. Pamene tinayamba ntchito yosindikiza kalata ya Chitamil: tinayambira ndi makalata okwana 500 kenaka nkumakula ndithu mpaka kufika pa 1,000, kenaka ndikudutsa kufika pa 2,000 ndipo tsopano pano tikusindikiza okwana 3,500. Izi zinatere chifukwa tinayamba kulandira makalata ndi matelefoni kuchokera kwa ena amene anatenga kalata ya Uthenga Wabwino wa Choonadi kapena anangomva kwa ena. Kuyambira nthawi imeneyo, pafupifupi makalata okwana 75,000 a chi Tamil atumizidwa.

Ndikhoza kuchitira umboni kuti ndaona chipatso cha mbeu za uthenga wabwino zomwe zabzalidwa kudzera mu makalatawa pa kumadera amene kumagwirika ntchito yolalikira uthenga wabwino. Ndili woyamika podziwa kuti Yehova akhoza kugwira ntchito ndi mbeu zimenezi kwa chaka chonse, kaya tikhalepo kumaloko kapena ayi. Njira zosungira makalata akale pa intaneti zakhalanso ngati kalozera wothandiza pophunzitsa chiphunzitso cha Baibulo pa nkhani zosiyanasiyana zimene zimabuka pamene ndinali nawo kumalo kolalikira uthenga wabwino. Ndikukulimbikitsani kwambiri kuti panokha mulembetse mu chiphunzitso cha Baibulo, kuti mukhale "okonzeka nthawi zonse . . . chifukwa cha chiyembekezo chili mwa inu" (1 Petro 3:15). Ndipo ndikukhulupirira kuti mudzapeza kalata ya Choonadi cha Uthenga Wabwino kukhala yothandiza kwambiri potsagana nayo paulendowu.

—Mbale Clint Doolittle



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

Mbiri ya Choonadi cha Uthenga Wabwino

Makalata onse za Gospel Truth alipo pa intaneti ndipo mukhoza kuwapeza pa www.thegospeltruth.org.

Panopa kalatayi ikupezeka m'zinenero zisanu ndi ziwiri.



1. Uthenga wabwino, Choonadi, Kuona mtima
2. Chipulumutso, Uchimo
3. Ubale wa Chikondi
4. Ufumu wa Mulungu
5. Za masiku otsiriza—Kubwera Kwachiwiri kwa Khristu, Nthawi za kumapeto
6. Mpingo wa Mulungu
7. Mphamvu ya chikoka, Mafilimu, TV
8. Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera
9. Glossolalia—Kulankhula M'malilime
10. Ubatizo wa Madzi
11. Mwambo wosambitsa mapazi; Kudzichepetsa
12. Mazunzo a Khristu; Mgonero wa Ambuye
13. Kudzilungamitsa
14. Kusudzulana ndi Kukwatiranso
15. Ntchito Zachifundo
16. Maonekedwe Akunja—Mavalidwe a Chikhristu
17. Utumiki
18. Mapangano Awiri
19. Chakhumi mu Baibulo ndi Kupereka
20. Sabata ndi Tsiku la Ambuye
21. Maimbidwe mu kupembedza
22. Utatu wa Mulungu
23. Ubwino wa Kudzisanthula wekha
24. Machiritso a Kumwamba
25. Kusala
26. Kusabwezera kwa Mkhristu
27. Kukhala mdindo pachuma
28. Chitetezo chamuyaya
29. Imfa ndi Kuuka, koyamba ndi kwachiwiri
30. Matamando
31. Pemphero
32. COVID-19 (Kalata yapadera)
33. Kupatulidwa ku Utumiki
34. Udindo wa Mtumiki
35. Osakhala a Dziko Lapansi
36. Mu nthawi za nsautso
37. Mphamvu ya Mafanizo
38. Kulapa
39. Kuona mtima
40. Mmene Mungadziwire Chifuniro cha Mulungu



Chingerezi



Chisipanishi



Chijeremani



Tamil



Chichewa



Swahili



Malayalam

Zochitika kuseri

Gulu losindikiza ndi kufalitsa kalata ya Uthenga Wabwino

Tithokoze mwapadera chifukwa cha kudzipereka komanso zaka zambiri zautumiki wa gulu losindikiza kalata ya Gospel Truth. Palibe chinthu chokoma kwa munthu ngati kuwerenga uthenga wabwino m'chilankhulo chako! Zinthu zimene zayikidwa pa webusayiti zikuyimira zaka zogwira ntchito komanso antchito odzipereka. Kalata ya Chingerezi ikatulutsidwa, omasulira ndi osindikiza athu amagwira ntchito yakuti kalata yatsopanoyi igawidwe padziko lonse. Malo osindikizira akhazikitsidwa m'maiko osiyanasiyana ndipo makalata zikwizikwi amasindikizidwa ndikugawidwa pamisonkhano ndi zilinganizo zofalitsa uthenga wabwino padziko lonse lapansi. Timalandira mapempho pafupipafupi kuti zinenero zatsopano ziwonjezedwe koma tikanali ochepekedwa chifukwa cha nthawi, ndalama komanso antchito. Tikuthokoza Mulungu chifukwa cha antchito athu okhulupirika!



Michael Smith

Mkonzi wamkulu



René Smith

Wokonza zonse/
Mkulu wa ntchito
yomasulira (USA)



Aubrey Sorrell

Maonekedwe
Akunja (USA)



Julie Elwell

Wowerenganso (USA)



Janet McMurrin

Wowerenganso (USA)



Lenée Sorrell

Webusaiti (USA)



Irma Sallee

Wowerenganso
(USA)



Damon Sallee

Wopanga ma
App (USA)



Vanessa Smith

Wotumiza makalata
(USA)



Tricia Bell

Womasulira
Chisipanishi (USA)



Adrian Glezs

Wowerenganso
Chisipanishi (Mexico)



Ariel Perez

Wowerenganso
Chisipanishi (Mexico)



Ludwig Laukert

Womasulira
Wachijeremani
(Germany)



**Barth
Nwachukwu**

Wosindikiza (Nigeria)



W. S. Vedha

Mkonzi wa ku Tamil/
Wowerenganso (India)



V. J. Gnanarajan

Chi Tamil
Wosindikiza/
Womasulira (India)



V. Selvam

Bungwe lotumiza
Makalata ku
Tamil (India)



**V. J. Sam
Kirubaharan**

Wotumiza makalata
ku Tamil (India)



Stephen Mwangi

Womasulira Chiswahili
(Kenya Bible Society)



Alice Ahuga

Wosindikiza wa
Chiswahili (Kenya)



Falistani Kansilanga

Chichewa
Womasulira/Wosindikiza
(Malawi Bible Society)



Matthew Joseph

Mkonzi/
Wowerenganso
Chimalayalam (India)



Baby Matthew

Wothandizira
Mkonzi/Womasulira
Chimalayalam (India)




Biju J. Varghese



Wosindikiza/
Woyang'anira
Chimalayalam (India)

Zaka Khumi za Kukhulupirika kwa Mulungu

Tinayamba kusindikiza makalata pa makina osindikizira aang'ono amene anali ochedwetsa. Iwo anali pa patebulo imene inali pachipinda chodyera. Makinawa amatenga maora 12 kuti amalize ndipo amafunika kumawayang'anira pafupipafupi.



AMBUYE ANAPEREKA LAMULO:
NCHACHIKULU CHIWERENGERO
CHA AMENE ABWERA
NDI UTHENGA."
SALMO 68:11



KUKONDWERERA TSIKU LOBADWA UTHENGA WABWINO WA CHOONADI!



“Nkoyenera kuthokoza Mulungu chifukwa chogwiriziza ntchito yofalitsa kalata ya Uthenga Wabwino wa Choonadi kwa zaka 10 zimenezi. Kuyambira pachiyambi, yakhala kalata yokonedwa, yotumikira pa maphunziro ndi ntchito za ulaliki. Zikhoza kuoneka kwa ife pano ngati kuti kulalikira kwathu sikokwanira ngati tilibe kalata yakuti tiwagawire anthu. Koma koposa zonse ndi chisomo choperekedwa kuti tisindikize ndi kufalitsa mosalekeza.”

Chinwendu Nwachukwu, Nigeria

“Happy Birthday Gospel Truth! Mwa njira imeneyi anthu ambiri afikiridwa, ngakhale amene ali kumadera akumidzi kumene sangathe kugwiritsa ntchito makina a intaneti. Kalata ya Uthenga Wabwino wa Choonadi, yokhala ndi mavesi omveka bwino, yatithandiza kufikira anthu 5,000 mpaka 7,000.

“Izi zapangitsa kuti anthu ambiri abwere ndi kudzapempha choonadi chokhudza mpingo wa Church of God. Tiyeni tigwirane manja ndi kupemphera kuti utumiki wa Uthenga Wabwino wa Choonadi ukule kwambiri ndi kupyola nyanja komanso kudutsa malire. Utumiki wa Uthenga Wabwino waChoonadi ukhale ndi moyo wautali!”

Peter Akweyona, Kenya

“Ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha dongosolo lake lopangitsa kuti kalata ya Uthenga Wabwino wa Choonadi isindikizidwe ndi kufalitsidwa. Pambali pa kuwerenga Baibulo, timapatula nthawi yowerenga ndi kutsatira mau a Mulungu kudzera mu zowerenga izi, komanso Uthenga Wabwino wa Choonadi umathandizira kufikira aliyense n'madera osiyanasiyana popanda kuwerengera ngati munthuyo ali ndi Baibulo kapena ayi.

“Uthenga Wabwino wa Choonadi umathandizira kusintha mitima ya anthu osiyanasiyana, ngakhale iwo amene sali mamembala a mpingo wathu wa Church of God. Kuno ku Malawi ndi ku Mozambique tikupemphera kuti Mulungu athandize kuti ntchito iyi yosindikiza mabukuwa ipitirire. Mulungu adalitse.”

Master Gustor, Malawi

“Tili pachikondwerero cha zaka 10 mwachangu kwambiri. Tinayamba ndi mabuku okwana 500 kenako mothandizidwa ndi oyera mtima tidaonjezera pang'onopang'ono mabuku athu mpaka 3,500. Izi zachitika ndi chisomo chodabwitsa cha Mulungu chokha.

“Makamaka, atumiki a Mulungu akugwiritsa ntchito uthenga umene uli mu Uthenga Wabwino wa Choonadi polalikira mu mapemphero awo a tsiku lamulungu. Pamene mtumiki akuwerenga, uthengawo udzafalikira kwa anthu a mumpingo kuti potero ukawafikire okhulupirira ena onse kudzera mwa mtumikiyo. Nthawi zambiri timagawira kalata ya Gospel Truth kwa atumiki a ku India.

Sikuti timangogawira anthu a ku Tamil ku India kokha komanso tikutumiza padziko lonse kumene anthu a ku Tamil akukhala. Pofuna kuti zinthu zipitebe patsogolo, pempherani kuti mabukuwa achuluke kuti tifalitse uthenga wabwino kwa anthu ambiri padziko lonse lapansi.”

WS Vedha, (Tamil Editor) India

“Ndithudi ndilibe mau osonyeza kuyamikira kwanga kwa Mulungu chifukwa cha kusindikizidwa kwa kalata ya Gospel Truth. Chiyambireni kusindikizidwa, ndimayiona kuti imalimbikitsa choonadi chimene chinaperekedwa kwa oyera mtima mu uthunthu onse. Mwachitsanzo: mu mphindi zochepa chabe, munthu akhoza kumvetsetsa bwino tanthauzo la choonadi chonse chimene chipezeka mu kalatayu.

“Kwa ife, njira imeneyi ndi yosavuta ndiponso yophweka pa zimene Baibulo limaphunzitsa. Kalatayi ikasindikizidwa, pambali pa kuyigawira ku mpingo wa Church of God, timaonetsetsa kuti aliyense payekha ali ndi kalata yake. Komanso kwakukulu timayigwiritsa ntchito mu maulaliki; ndipo timagawira iwo amene timakumana nawo, nyumba ndi nyumba mu njira ndi mu msewu, monga ngati njira imodzi yofalitsira Uthenga Wabwino pafupi komanso kutali. Imeneyi inali njira imene tinagwiritsira ntchito polalikira kumapeto kwa sabata yatha ku Tombia, River State.

“Timayigwiritsanso ntchito kawirikawiri mu masukulu athu a Sande, mu maphunziro a Baibulo, pa mwambo woika maliro, miyambo ya ukwati ndi zina zotero. Monga mmene ndinanenera nthawi ina m'mbuyomo, ndayamba kutumiza makalata a Gospel Truth omangidwa m'mapukutu kwa atumiki a Mulungu okwana asanu. Ndipo tidzapitirira kuchita izi monga mmene Yehova adzapereka. Pamene mukupitirizabe kuyatsa moto, musalole kuti uzime.”

Bro. Barth. CN, Nigeria



KODI MUKUDZIWA?

Padziko lapansi pali magulu a anthu okwana 17,400. Mwa iwo 42.1% sanafikiridwe ndi uthenga wabwino. India, Pakistan, ndi China ndi maiko atatu amene ali ndi magulu a anthu ochuluka kwambiri amene sanafikiridwe. Pali anthu ambiri masiku ano amene sadziwa Khristu kuposa nthawi ina iliyonse mu mbiri ya dziko.

Source: Joshua Project 2022



Mau a Nyengo Yake

MAU OTENGEDWA KU MAKALATA AKALE

“Pali kusinthika kodabwitsa kumene kumachitika pamene munthu wina wapulumutsidwa kwenikweni kudzera mu mphamvu ya Yesu Khristu. Mkhristu—amene ali ophunzira wa Yesu Khristu, angathe kutsata chitsanzo cha chake cha Khristu ndi kukhala moyo wosachita uchimo (1 Petro 2:21-22). Anthu ambiri achipembedzo basi amachipeputsa choonadi chooneka ngati chopusachi nkumanyengezera kuti chimenechi sichilungamo.” *Kalata Yachiwiri, Uchimo ndi Chipulumutso.*

“Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi ntchito ya chikhulupiriro ndipo nthawi zonse sizichitika ndi ziwonetsero zazikulu kapena mmene munthu akumvera.”...“Chitsimikizo chenicheni cha Mzimu Woyera ndiko kuthekera ndiponso mphamvu yokhala moyo wachiyero.” *Kalata ya 8, Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera.*



“Matamando opita kwa Mulungu kudzera mu kufuula, kuperekera umboni, kapena kuimba nyimbo amatsekula zipata zokafika pamaso penipeni pa Mulungu, popeza Mulungu amakhala m'matamando.” *Kalata ya 30, Matamando.*

“Temberero la uchimo linali imfa ya kuuzimu ndi kuthupi.”...“Chilango cha imfa yakuzimu chinasinthidwa kupyolera mu chikhululukiro ndi chiweruzo cha Yesu Khristu.” *Kalata ya 29, Imfa ndi Kuuka, Koyamba ndi Kwachiwiri.*

“Ifeyo pokhala adindo a Mulungu, tikuyenera kuti ndalama zathu tizilamulire ndi kuziyang'anira ndi chisamaliro komanso kukhulupirika komweko monga m'mene timachitira ndi zinthu zauzimu.” *Kalata ya 27, Kukhala mdindo pachuma.*

“Pali kusiyana kwakukulu pakati pa zofuna za ana a Mulungu amene akukhala pansu pa chisomo ndiponso udindo umene Mulungu waika pa maulamuliro a dziko lapansi amene akulamulira mwathupi.” *Kalata ya 26, Kusabwezera kwa Mkhristu.*

“Popanda kudzisanthula wekha mu kuopa Mulungu, munthu akhoza kudzinamiza. Sikokwanira kungomva Mau kokha, tiyenerakukhala anthu ochita Mau apo ayi.” *Kalata ya 23, Ubwino wa Kudzisanthula wekha.*

“Sabata ya Chikhristu yeniyeni mu nthawi ya Chipangano Chatsopano ndiyo ya mtendere, mpumulo, kupembedza kwa uzimu, ndiponso kukhala moyo wachiyero tsiku lililonse la sabatalo. Tsiku lililonse ndi lopatulika ndiponso lisungidwe kukhala lolingalira ndiponso kukumbukira kuombedwa ku uchimo kudzera mwa Yesu Khristu.” *Kalata ya 20, Sabata.*

“Nkofunika kufunafuna chifuniro cha Mulungu pamene tikuyenda m'moyo wa kumvera m'magawo onse a moyo. Sitingayembekeze kuti Mulungu adzaulula cholinga chake m'gawo lina malinga ndi zofuna zathu ngati sitikumvera zimene tikudziwa kuti ndi chifuniro chake m'mbali zina.” *Kalata ya 40, Mmene Tingadziwire Chifuniro cha Mulungu.*

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE